WEEKEND NATION
LOWERUKA, 23 DECEMBER 2023



Matchera amene akumangidwa popatutsa mtsinje wa Shire



Kuthira fetereza kunja kudakali ng'amba kumachititsa kuti feterezayo aziyamwa chinyontho m'mbewu chifukwa m'dothi kumakhala mulibe chokwanira. Kupalira motsegula mizere kumakhala ngati kuyanika dothi choncho chinyontho chochepetsetsa chimene mbewu zidakagwiritsa ntchito mwina ndi kupulumukako chimathamo.—*A Frank Kaulembe, mlangizi wa mbewu kwa Bvumbwe*

# Ateteza nsomba ya mtundu wa kambuku

WOLEMBA
**MARTIN GELA**

Ngati mbali imodzi yoonetsetsa kuti chitukuko cha mgula wa madzi a mthirira omwe boma la Malawi likumanga kuchigwa cha mtsinje wa Shire kudzera ku Shire Valley Transformation Programme (SVTP) chipindulire anthu kwa muyaya, boma likuonetsetsa kuti chilengedwe chisamalidwe pamene ntchitoyi ikugwiridwa.

Njira imodzi imene boma lapanga kuti izi zitheke ndi kumanga tchingo loteteza kuti nsomba ya mtundu wa kambuku isadutse mgulawu.

Mneneri wa pulojekiti ya SVTP mayi Alice Kaunda anati nsomba ya mtundu wakambuku yomwe imapezeka mumtsinje wa Zambezi ndi yovuta kwambiri chifukwa imadya nsomba zinzake.

"Tamanga tchingoli ndi cholinga choteteza nsomba ya mtundu wa kambuku imene m'Chingerezi imatchedwa *tiger fish* kuti isadutse n'kulowa mumtsinje wa Shire kenaka kukafika ku nyanja ya Malawi chifukwa ikhoza kusakaza nsomba zathu za mtengo wapatali," adatero a Kaunda.

Iwo adati nyanja zathu zimadziwika ndi mitundu ya nsomba zosiyanasiyana zina zomwe zimapezeka kwathu kokha kuno padziko lonse lapansi. Nsomba zina zotchuka ndi mbuna, chambo, mcheni, ntchira, sanjika, kadyakolo, ndi mbaba.

"Zonsezi zikhoza kukhala mbiri yakale ngati nsombazi zitafika m'nyanja yathu ya Malawi. Ichi n'chifukwa chake tinaganiza zomanga malo ano," adatero iwo

Mmodzi mwa asodzi a m'nyanja ya Malawi a m'mudzi wa Chirombo T/A Nankumba ku Mangochi a Yohane James anayamikira ganizoli lomwe liteteze nsomba ponena kuti izi ndiye mgodi wawo.

Ndipo ochokera ku kampani ya Ripple Africa yomwe imateteza nsomba m'dziko muno makamaka za mtundu wa mbuna a Sam Manda anayamikiranso ganizoli.

"Onse omwe akupanga zitukuko zosiyanasiyana akuyenera kuika patsogolo momwe angatetezere zachilengedwe kuphatikizapo nsomba," adatero iwo.

Iwo adati pamenepa boma kudzera ku SVTP lidaganiza bwino kuti pamene miyoyo ya anthu ikhale ikutukuka kudzera ku ulimi wa mthirira, zachilengedwe kuphatikizapo nsomba zitetezedwe ku zinthu zoononga monga mtundu wa nsomba wa kambuku," adatero a Manda.

Boma kudzera ku unduna wa za ulimi likumanga mgulawu omwe ndi wa makilomitala 118 kuchokera ku damu la Kapichira ku Chikwawa kukafika ku Bangula m'boma la Nsanje, ntchito yomwe idzapindulire mabanja oposa 48 000 kuchokera ku mahekitala 43 370. ■



ZITHUNZI: MARTIN GELA

Nsomba ya kambuku imadya nsomba zinzake

"

*Minda imene tidabzala mbewu zidamera ndithu koma kupitamo padakali pano simukuonekanso kuti mudabzalidwa choncho tangotaya tidzachita kuyambiranso. Anthu adali ndi chiyembekezo kuti pofika pano ntchito zopalira m'minda zikhala zitagundika ndipo azipeza ndalama yogulira chakudya koma padakali pano akusowa mtengo wogwira.,*

"

TUMIZANI MAGANIZO NDI MAFUNSO ANU

Lemberani kwa: Mkonzi, Uchikumbe, P. O. Box 30408, Chichiri, Blantyre 3. Tumizani uthenga pafoni ku 0888412807.